

## KUTSATIRA YESU KRISTU

Pamene Ambuye Yesu anali pa dziko la pansi, asanapachikidwe pa mtanda, komanso asanauke m'mwambamwamba anati kwa ophunzira ake' **"Nditsateni ine"**, (Yohane 1:43)

Yohane m'batizi ndi amene adayamba kudziwa ndikunena kwa anthu kuti; "Onani mwana wa Nkhosa wa Mulungu amene achotsa tchimo la dziko la pansi, wotumizidwa ndi Atate a kumwamba". Pamene ophunzira awiri amene adali ndi iye atamva izi adamusiya Yohane ndikutsata Ambuye Yesu. Andreyo m'modzi mwa ophunzira ake anampeza Simoni nati; "Tapeza ife Kristu", Petro anamtsatanso Yesu. Filipino anapita nampeza Natanayeli namuuzza kuti "tampeza munthu amene Mose ndi Aneneri ananena za Iye", ndipo Natanayeli atafika kwa Yesu anati; "M'phunzitsi, inu ndinu mwana wa Mulungu, Mfumu ya Israeli", (Yohane 1:35 – 45). Ambuye Yesu atakumana ndi ana a Zebedayo, ndipo ataona zodabwitsa anasiya zonse adali kuchita ndikumtsata Iye, (Luka 5). Komanso M'buku la Mateyu, Yesu anati kwa Simon ndi Andreyo; **"Nditsateni ndipo ndidzakusandutsanu asodzi a anthu"**, (Mateyu 4: 19 ). Anatinso kwa Mateyu wokhometsa msonkho; **"Nditsate ine"**, (Mateyu 9:9). Pamene tikuona kuti Ambuye Yesu ndi "M'phunzitsi" komanso "Kristu" munthu amene Mose ndi Aneneri anayankhura za Iye m'malemba a chipangano cha kale, kuti ndimwana wa Mulungu, Mfumu ya mafumu, Mbuye wa a mbuye.

Pamene tikuonanso kuti onse amene anaitanidwa ndi Ambuye Yesu ndikumtsata, iwonso anaitana anzawo ndikumtsata Ambuye Yesu. Panalibe munthu amene amatsata munthu mnzache, koma onse amatsata Ambuye Yesu Kristu.

Apa tikuona kuti Ambuye Yesu sanawetengere anthuwa chipembedzo cha dzina lina kapena Mpingo uli onse, kapena kwa munthu aliyense wozozedwa wopanga zozizwa, kapena kutsata malamulo ena abwino a dziko la pansi, koma anaitana iwo kwa Iye yekha kuti amtsate Iye. Ambuye Yesu anali munthu ngati ife. Anthu onse amene anamkhulupilira anamtsata Iye ndi mtima umodzi ndi cholinga chimodzi. Ngakhale m'mene Yudas anayamba kuchita malingaliro opereka Ambuye Yesu kwa adani ake, panalibe m'modzi mwa ophunzira enawo adatsatira maganizo oipa a Yudas chifukwa onse amakhulupilira Ambuye Yesu osati m'khiristu mnzao. Onse okhulupilira anthu anzawo amagwa pamene yemwe amam'khulupilirayo wagwa. Khulupilirani Yesu sadzakukhumudwitsani.

Choncho Ambuye Yesu analamula onse omtsata Iye ndikuti; "Ngati munthu afuna kunditsata ine, adzikane yekha(kusiya machimo) ndikunyamula mtanda wache tsiku ndi tsiku ndikunditsata", (LUKA 9:23).

Pamene Ambuye Yesu Kristu analamura kwa iwo kuti "munditsate ine" anali atachita kale zozizwa, ndikuwauza ophunzira ake kukhala moyo wachilungamo, ndipo iwo anasiya zonse zawo ndikutsata Ambuye Yesu tsiku ndi tsiku. Ambuye Yesu anati

kwa gulu lonse; “Dzikaneni nokha, kusenza mtanda ndikunditsata ine”, ( Maliko 8:34)

## **KODI MTANDA N’CHIYANI?, N’CHIFUKWA CHIYANI AMAFUNSIDWA KUNYAMURA MTANDA?, NANGA MTANDA TINGAWUNYAMURE BWANJI?**

Mtanda ndi mayesero amene timakumana nawo muchukhirisitu chathu, amene tiyenera kuwapilira tsiku ndi tsiku. Pamtanda ndi pamene ankapherapo anthu opanga zoipa ndi oswa lamulo (Luka 23:32). Mchipangano chakale munthu wopachikidwa pa mtanda amatchulidwa wotembeleredwa ndi Mulungu (Detronome 21:23). Ichi ndichifukwa chake Ambuye Yesu Kristu anatiombora ku thembelero la lamulo, nakhala thembelero m’ malo mwa ife, (Agalatiya 3:13). Ambuye Yesu ameneyu sadziwe tchimo, anatumizidwa kudziko kudzapanga chifuniro cha Atate, osapanga chifuniro cha moyo wache. Ananyamula mtanda, anakumana ndi mazunzo owopsa mwachikonzero cha Mulungu. Anapyola m’minyozo, anamenyedwa, natunduzidwa ndi kunyozedwa koma sanabwezere. Anafa imfa ngati munthu opanga zoipa ngakhale anali wa chilungamo, woyera, wopanda banga. Anafa chifukwa cha machimo athu amene tinachimwira Mulungu, nasenza thembelero lathu paphewa pache. Awa ndi matembelero amene anayenera kufika pa ife chifukwa cha uchimo.

Tikudziwa kuti munthu sangafe kudziombora yekha ku machimo ake kapena kuombora a anzathu. Kodi nanga kusenza mtanda nkutani?; uku kumatanthauza kusiya maganizo athu, njira zathu ndi mapulani athu ndikutsata chifuniro cha Mulungu chokha. Komanso tichiyese chimwemwe pamene tikumana ndi mavuto osiyanasiyana mwa Ambuye, (Yakobo 1:2). Komanso kukhala m’ mawu a Mulungu ndikuyenda motsogozedwa ndi mawu achi ndi chifuniro chache ng akhale ena atinyoze, ngakhale tikhale ngati opeputsidwa, osadziwika kudziko la pansu, monga Ambuye Yesu anati ; “Ngakhale dziko lindinyoze, ndidzachitabe chifuniro chanu Atate, osati chifuniro chake,(Luka 22:42). Ngakhale m’buku la Masalimo 40:8 anati; “ kuchita chikondwero chanu kundikonda, Mulungu wanga; ndipo malamulo anu ali mkati mwamtima mwanga.

Mulungu anakonza kuti Yesu akhale “Nsembe” ya mwana wa “Nkhosa” imene ikaferere pa mtanda kuti atafa adzaukenso ndikupereka moyo kwa onse okhulupilira lye, (Yesaya 53). Ndipo kuti pamene ataukitsidwa akakwezedwe, ndikupereka mphatso za Uzimu kwa abale ambiri amene alora kuti Kristu akhale mwa iwo, ndikutsogozedwa ndi Mzimu Oyera . Kodi nanga Ophunzira a Yesu amatha bwanji kukana tchimo pamene nawonso anali ndi thupi ngati ife?, Kodi zinali zophweka kunyamula mtanda umene umaimilira machimo ndi chiweruzo cha Mulungu mwa iwo wokha, ndi kudzifera okha? Ayi nkosatheka!! Izi n’zosatheka munthu kudzifera yekha, ndi Yesu yekha akanakhoza kuferera anthu onse ndi Ophunzira achi omwe. Imfa yathu ndi ya Ophunzira achi, machimo awo ndi machimo athu, akuwerengedwa mwa Ambuye Yesu. Chilango chimene chikanatigwera ife chinagwera pa Ambuye Yesu Kristu, ndipo ananyamula zonse pa mtanda.

Pamene Yesu Kristu anaukitsidwa kwa akufa anatipatsa thupi latsopano limene linalengedwa mchifaniziro cha Mulungu mwachiyero ndi mwachilungamo. Koteroko moyo watsopano tidaulandira pakuuka kwake monga akunena m’buku la 2 Akorinto 5:17; “Aliyense amene ali mwa Kristu ali olengedwa watsopano, zakale zapita, taonani zikhala zatsopano”.

Ambuye Yesu atauka kwa akufa, anakwera m'mwambamwamba natipatsa Mzimu Oyera amene amatipatsa mphatso za Uzimu ndi chidziwitso chenicheni chimene tili nacho mwa Kristu. "Ndipo Kristu atakwezedwa kumwamba kumpando wachifumu, kudzanja la manja la Atate adatilonjeza kutitumizira ife Mzimu Oyera", (Machitidwe Atumwi 2:33).

Choncho ngakhale Yesu analamula kuti; "Tidzikanize tokha ndikusenza mtanda wathu tsiku ndi tsiku ndi kumtsata lye", ndizinthu zosatheka patokha, makamaka tiziwerengere wofaifa ku uchimo ndi ku lamulo mwa Yesu Kristu (Aroma 7:4 – 6). Ndi chifukwa choti tinaukitsidwa ndi iye ndikulandira moyo watsopano mwa Kristu Yesu natipatsa Mzimu Oyera, pamenepo ndiye kuti tinafa ndi lye, tiziwengere tokha akufa ku uchimo ndi kuti umunthu wathu wakale wa uchimo unapachikidwa ndi Yesu pa mtanda ndipo anatipatsa moyo watsopano pakuuka kwake.

Kodi kunyamura mtanda kutanthauzani kwa ife?; zikutanthauza kumutsata Yesu tsiku ndi tsiku ngakhale pa mavuto ndikuyenda moyo watsopano mwa Yesu motsogozedwa ndi Mzimu Oyera. Kupitilirabe kuphunzira mawu a Mulungu ndi kumvera malangizo ake onse amene tiwamva, osatsata maganizo athu oipa, kusiya njira zathu zoipa ndi kulora kufuna kwa Mulungu kuchitike pa ife. Kulora kuyenda mmavuto potumikira anzathu, osatsata zabwino zokhazokha, chimenechichi ndiye chikhulupiliro chenicheni cha mtengo wapatali kuposa ndalama, (1 Petro 1:7).

Umunthu wathu wakale wa Uchimo ndi kupanduka kwathu kwa Mulungu zinachotsedwa ndi Yesu Kristu. Ndipo madalitso a Uzimu, moyo watsopano mwa Kristu Yesu, chilungamo ndi mtendere, chimwemwe, chikondi mwa Mzimu Oyera chatipatsa ife mphatso zaulere. Choncho tisankhe kuyenda mchisomo chimenechi tsiku ndi tsiku.

Choncho mmene Yesu amaitanira Ophunzira ache sizinasinthe; paja ankati kwa aliyense "Nditsate ine". Bvuto lilipo masiku ano anthu akutsata ziphunzitsa za anthu osati Yesu. Tichenjere ndi anthu amene ayankhura mochenjera ndikuyara mfundo zawo bwino, azozizwa, ndithu owoneka kuti ozozedwa koma mukawayang'anitsitsa Sali kupanga za Yesu koma za ziwanda ndi kufuna kukhutitsa mimba zawo. Yesutu ndi Mpulumutsi wathu, M'phunzitsi, mwana wa Mulungu ndi Mfumu ya mafumu yokhala mwa ife, tinakhulupilira Yesu, tiyenera kumtsatira iye yekha basi. Monga aneneri akale amaimilira m'malo mwa Yesu monga; Mose, Eliya, Isaki, Samueli, Davite, Adam ndi ena otero. Kotero ndikupemphani kuti tisasiye kutsatira Yesu amene ali Mpulumutsi wathu, Mneneri, Mfumu, Mbuye, Woweruza wathu, Wansembe, Mutu ndi mtsogoleri wathu.

Mulungu watipatsa ife Yesu Kristu monga mphatso yokhala mwa ife mwa Mzimu Oyera kuti tikazikanize tokha ndi kusenza mtanda wathu, ndi kumtsata iye tsiku ndi tsiku. Osatsata zinthu zabodza ayi. "chifukwa chake monga munalandira Kristu Yesu Ambuye muyende mwa lye", (Akolose 2:6). "Koma ndinena, muyendeyende ndi Mzimu, ndipo musafitse chilakolako cha thupi", (Agalatiya 5:16). "Koma bvalani inu Ambuye Yesu Kristu, ndipo musaganizire za thupi kuchita zofuna zache", (Aroma 13:14).

Chotero siyani ntchito zanu zakufa zakale, zimene zinapita ndi umunthu wakale, zimene zinapachikidwa ndi Kristu Yesu pa mtanda. Kotero onse amene anabatizidwa ndi Yesu anapachikanso ndi ntchito zawo zomwe. Monga Yesu anafa kamodzi popachikidwa pamtanda, choncho ifenso sitiyenera kubwelera kumachimo

athu kachiwiri. Kubweleranso ku machimo kuli ngati kufanso kachiwiri. Monga Yesu anaukutsidwa nakwera kumwamba, adapanga miyoyo yathu kukhala mokhalamo lye mwa Mzimu Oyera. Chotero yendani ndi Yesu kristu.

Kusenza mtanda ndikutsata Yesu tsiku ndi tsiku kukutanthauza kuyenda molingana ndi chifuniro cha Mulungu komanso kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera. Potsatanso nzeru yawekha. Munthu akalora Mzimu woyera kuti umutsogolere, mtendere wa Mulungu umalamulira mu mtima wache; " koma ndinena, muyendeyende ndi Mzimu ndipo musafitse chilakolako cha thupi", (Agalatiya 5:16).

Pamene Ambuye Mulungu anapulumutsa ana a Israeli mdziko la Egipto ndikuwalowetsa mu Kenani, dziko la mpumulo sanaononge msanga adani awo onse. Anasiya ena osawapha kuti aphunzitse Israeli kamenyedwe ka nkondo kuti aone ngati angaphunzire kuopa ndi kumvera Mulungu (Oweruza 3: 2 – 4 ). Chomvetsa chisoni nchoti pasantenge nthawi Israeli Anayamba kusamvera Mulungu ndikutsata njira za mitundu ina imene idawazungulira iwo.

Umunthu wathu wakale wachikunja unatha, pamenepo ndife olengedwa m'moyo watsopano mwa Yesu Kristu. Tikayang'ana m'mbuyomu kwa Israeli ndi phunziro kwa ife kuti ngakhale takula mu Uzimu, sitinadziwebe dalitso la Mulungu limene lili mwa Kristu Yesu. Tisasakanize umunthu wathu wakale ndi watsopano, simungasakanize moyo ndi imfa. Tiyeni tidzimvera Atate Mulungu kuti tikayende mwa lye ndi kukula limodzi mwansanga ku muyeso wa usinkhu wa Kristu Yesu. Tisasakanize udani ndi chikondi, kunyada ndi kudzichepetsa, chikhululuko ndi kusakhululuka, mkwiyo ndi chimwemwe, chilungamo ndi kusalungama chifukwa zonsezi ndizikhumbitso za thupi. Tiyen tilore kutsogozedwa ndi Mzimu Oyera kuti akatidziwitse adani achikhrisitu ndi zimene tiyenera kuzichotsa muntima mwathu, kuti ntchito zokufa zisabisale m'moyo mwathu. Nthawi zina Israeli amatenga adani ake osawapha, mmalo mwache awapanga kukhala akapolo awo kuti adziwagwilira ntchito, chimene sichinali chifuniro cha Mulungu, koma chifuniro cha Mulungu chidali choti Israeli athamangitse adani ache onse mdzikomo, (Oweruza 1:19 - 36). Mulungu analonjeza kuti adzathamangitsa adani lye yekha, kuti Israeli amvere malamulo ake bwino,(Eksodo 23:20 - 32). Tiyeni tikumbukire kudalira pa Mzimu Oyera ndikuyenda mu chifuniro chake kuti lye athamangitse adani m'mitima yathu. Zimenezi sizingatheke kuchita tokha, tikatero tidzalephera monga Isareli ndikukhala monga mwa thupi koma chikhalirocho tili aKhrisitu, (1 Akorinto 3:3). Tiyenera kudziwa kuti; "koma iwo a Kristu Yesu adapachika thupi ndi zokhumba zache ndi zilakolako zache", (Agalatiya 5:24). Tiziwerengere tokha opachikidwa ndi Kristu, kulandira moyo watsopano mwa ulemelero wa Kristu, tiyeni tidalire Mzimu Oyera.

Mulungu kachiwiri analamulira Israeli kuti asatengere makhalidwe ndi njira za achikunja amene ali pakati pawo, (Eksodo 23;20 - 23). Masiku ano tikuona a Kristu kapena kuti Mpingo wa Ambuye Yesu Kristu akutengera makhalidwe adziko monga; kukonda chuma, kudzitsogolera okha, ena amatsatira anthu anzawo osati Yesu, ena amakhulupilira mipingo yawo kuposa Yesu. Mtumwi Paulo anafunsa kuti; " Pakuti pokhala pali nkhwidzi ndi ndeu pakati pa inu simuli athupi kodi, ndi kuyendayenda monga mwa munthu?, pakuti pamene wina anena, ine ndine wa Paulo, koma mnzache ndine wa Apolo; simuli athupi kodi?", (1 Akorinto 3:3 - 4). Pamenepo Mneneri kapena m'busa ali kuti amene mumamkhulupilira? ndipo alipo mwa iwo amene anapachikidwa chifukwa cha machimo anu? kapena munabatizidwa mdzina lawo?. Koma kwa ife monga Mpingo wa Ambuye tiyenera kukhala amodzi,

ogwirizana mucholinga cha Mzimu Oyera, muchilangizo chimodzi monga anachitira nd Isareli, “Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano: koma mukhale osandulika mtima wanu, kuti mukazindikire chimene chiri chifuniro cha Mulungu, chabwino ndi chokondweretsa ndi changwiro”, (Aefeso 12:2)

Mutatha kusiya umunthu wauchimo ndi mayesero amene amadza ndi misampha ya satana m’diyerekezi; “Nimuvale munthu watsopano, amene analengedwa monga mwa Mulungu, m’chilungamo, ndi mchiyero cha choonadi”, (Aefeso 4:24 ndi Akolose 3:10).

## **KUYENDA NDI MZIMU**

“Ndipo mu kudzodza kumene munalandira kuchokera kwa lye, kukhala mwa inu, ndipo simusowa kuti wina akuphunzitseni; koma monga kudzodza kwache kukuphunzitsani za zinthu zones, ndipo kuli koona, sikuli bodza monga kudaphunzitsa inu, mukhale mwa lye”,(1 Yohane 2:27).

Mzimu Woyera amakhala muntima mwa aliyense wokhulupilira, wam’ng’ono ngakhale wamkulu. Tonse tinalandira Mzimu m’modzi yemweyo mofanana, kaya oyamba kale kukhulupilira ngakhale oyamba kumene. Choncho ngati Mzimu yemweyo ali mwa aliyense, ameneyo ndiye “M’phunzitsi” wamkulu wotiphunzitsa tonse; wam’ng’ono ngakhale wamkulu. Pali anthu ena omwe ali ndi mphatso yophunzitsa amene akhulupilira kumene kumvetsa mawu a Mulungu. Motero anthu ophunzitsawa asalowe m’malo mwa Mzimu Woyera(Yesu).

Ngati tilora anthu kuti alowe m’malo a Mzimu Woyera(Yesu) ndikumagwira ntchito za Mzimu Woyera, ndikumatiuza za maganizo awo, chiphunzitsocho sichamulungu koma cha ziwanda cha Nikolayi chimene chimaletsa aKhirisitu kukura mwa Mzimu. Pamene ophunzitsa mawu aphunzitsabe aKhirisitu mpaka kalekale, aKhirisituwa samakura ku Uzimu, koma pamene aphunzitsa mawu, kenako ophunzirawo ayambe kuchita zomwe akuphunzirazo ndikuyamba nawonso kutsogozedwa ndi Mzimu amene amatsogoleranso ophunzitsawo. Asamangodikira munthu m’modzi kuti agwire ntchito zones pa Mpingo, ndiye kuti Mpingowo sungakure msanga. Tiyeni tikure, tisangokhalabe makanda.

Pamene Ophunzira anaitanidwa ndi Ambuye Yesu, anamudziwa Yesu monga Mpulumutsi namutsata lye, nawalonjeza kuwatumizira Nkhoswe, ndiye Mzimu wachoonadi. “Ndipo ine ndidzapempha Atate ndipo adzakupatsani inu Nkhoswe yina, kuti akhale ndi inu ku nthawi yonse, ndiye Mzimu wachoonadi; amene dziko la pansi silingathe kumlandira lye, chifukwa akhala ndi inu, nadzakhala kwa inu”, (Yohane 14:16 – 17). Ambuye Yesu anauka kwa akufa, nakwezedwa kukakhala ku malo opaturika ku dzanja la manja la Atate, choncho mmene analonjezera lonjezano la Mzimu Woyera ponena kuti; “Koma ndinena lne choonadi ndi inu; Nkhosweyo sadzadza kwa inu; koma ngati ndipita ndidzamtuma lye kwa inu”, (Yohane 16:7). Ndipo Yesu anati; “ Kuyenera kwa inu kuti ndichoke ine; pakuti ngati sindichoka, Nkhosweyo sadzadza kwa inu”, (Yohane 16:7b). Buku la Machitidwe a Atumwi linayamba ndi kunena za mapitidwe a Yesu kumwemba monga akunena mu Machitidwe a Atumwi 1:9; “Ndipo m’mene adanena izi, ali chipenyere iwo, ananyamulidwe; ndipo mtambounamlandira lye kumchotsa kumaso kwawo”. Mu chaputara chachiwiri cha Machitidwe a Atumwi akuti; “Ndipo anadzadzidwa onse ndi

Mzimu Woyera, nayamba kulankhura ndi malilime ena monga Mzimu anawayankhulira”, (Machitidwe a Atumwi 2:4).

Kodi ntchito ya Mzimu Woyera ndiyotani?, monga tikumva kuti Yesu atalandiridwa m'mitambo kukwera kumwamba (Machitidwe a Atumwi 1:19), ndipo onse Ophunzira a Yesu anasonkhana pamalo amodzi, ndipo onse analandira Mzimu Woyera, pamene Petro anaimilira nayankhura ndi mphamvu ya Mzimu Woyera ndikuti; “Potero, popeza anakwezedwa ndi dzanja la manja la Mulungu, nalandilidwa kwa Atate lonjezano la Mzimu Woyera, anatsanulira ichi, chimene inu mupenya nimumva”, (Machitidwe a Atumwi 2:33).

Onse analandira Mzimu Woyera chifukwa Yesu anakwera kumwamba. Anthu akuyang'anayang'ana zizindikiro za malandilidwe a Mzimu Woyera koma sayang'ana zizindikiro zakuyenda ndi Mzimu Woyera, ena amangodalira kuyankhura malilime koma zoti azindikire kuti Mzimu Woyera ali mwa iwo kuti awatsogolere alibe nazo ntchito. Zoonadi anthu ayenera kulandira Mzimu Woyera nayankhura malilime monga Petero anaimilira nalongosola zimene zinanenedwa kale ndi Mneneri Yoweli; “Ndipo kudzali m'masiku otsiriza, anena Mulungu, ndidzathira cha Mzimu wanga pa thupi liri lonse, ndipo ana anu amuna, ndi akazi adzanenera, ndipo anyamata anu adzaona masomphenya ndi akuru anu adzalota maloto”, (Machitidwe a Atumwi 2:17 ndi buku la Yoweli 2:28 – 32). Mneneri Yoweli anayankhura za Mzimu Woyera kuti udzapatsidwa kwa anyamata m'masiku otsiriza nadzaona maloto ndi masomphenya, zimene zinayambila ndi Ophunzira a Yesu atatha kulandira Mzimu Woyera nayamba kumalota maloto ndi mphatso zambiri zozizwa, (Yoweli 2:30).

Momwemo monga zinaliri ndi Ophunzira a Yesu, ifenso tikhale nacho chidziwitso mwa Mzimu Woyera amene akhala mwa ife. Tiyeni tiyang'ane pa lye kuti atidzale ndi kutitsogolera, ndikutiyang'anira, ndikutiphunzitsa zenizeni za moyo wa Yesu.

## **PENTEKOSITI**

Pa tsiku la Pentekositi ndi pamene Mpingo unayamba; umene uli thupi la Kristu, ndilo tsiku limene Ophunzira a Yesu analandira Mzimu Woyera. Petro yekha ndi amene anaimilira ndikuyankhura, zimenezi lero lino zawononga anthu ambiri amene amaganiza kuti munthu m'modzi yekha ndiye wamkulu ndipo ayenera kumalalikirira yekha mu Mpingo, zimenezi sizikuyenera kukhala choncho. Mpingo uyenera kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera osati munthu; anthu ndi atumiki chabe. Ndipo Atumwi onse atazazidwa ndi Mzimu Woyera nayamba kuyenda ndikuchitira umboni monga Mzimu Woyera anawatsogolera, sikuti Petro ndiye amatsogolera anthuwo koma ndi Mzimu Woyera.

Pamene Mpingo wasonkhana pamodzi, sindiye kuti udalire munthu m'modzi ayi, koma wina ngati ali nayo nyimbo ayimbe, wina aphunzitse, kaya wina mavumbulutso anene, kaya wina ayankhura malilime ayankhure ndi wina amasulire chimene chanenedwa kuti zikalimbikitse Mpingo, (1 Akorinto 14:28).

Pamene Mzimu Woyera ali pa onse, ndiye kuti Mpingo wonse umvere Mzimu Woyera ndi anthu onse atsogozedwe ndi Mzimu Woyera monga mwini Mpingo osati munthu.

Poyamba penipeni abale amene ali akulu mu Uzimu monga Atumwi, Aneneri, Alaliki, Abusa ndi Aphunzitsi amenewa ayenera kuphunzitsa anthu mawu a Mulungu, (Aefeso 4:11). M’Kristu aliyense ayenera kumakura mwa Ambuye Yesu Kristu chifukwa Yesuyo ndiye mutu wa Mpingo; “kuchokera mwa lye thupi lonse, lokowanidwa ndi lolumikizidwa pamodzi, pothandizanapo mfundo yonse, monga mwa kuchititsa kwa chiwalo chonse pa muyeso wache, lichita makulidwe a thupi, kufikira chimango chache mwa chikondi”, (Aefeso 4:16).

Abale takhala tikunamizidwa mokwana, tsopano ndi nthawi yoti ife tidziwe zenizeni zoposa Pentekositi. Pamenepo ndi nthawi yoti Mpingo ukure limodzi m’chigwirizano, chikhulupiliro ndi mchidziwitso cha mwana wa Mulungu. Makulidwe a mwa Ambuye kumuyeso wa Kristu ndi kuti aliyense mu Mpingo onse adzitsogozedwa ndi Mzimu Woyera umene tili nawo m’moyo wa Kristu. Pamenepo mwa Kristu mulibe wina wongoonelera kapena ndikumati ine simnadzozedwe koma awo okha, Mzimu Woyera ndi watonse ndipo ali mwa ife tonse Okhulupilira.

KHOTSO MOKOENA – 2016.